# Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

**Za kukwera Kumwamba kwa Yesu ndi kutumidwa kwa Mzimu wake Woyera**

1. Yesu anapita Kumwamba
2. Mzimu Woyera ali ndi nchito yapadera
3. Mzimu Woyera analimbikitsa ophunzira kuti ndiwo olimba mtima
4. Mzimu Woyera anaunikira ophunzira
5. Mzimu Woyera amakulitsa Mpingo wa Mulungu

# 1. Yesu anapita Kumwamba

*Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi Mateyu 28.18b*

**Kuwerenga**
Mateyu 28.16-20

**Malongosoledwe**
Kodi Yesu ali kuti tsopano? Ndi cifukwa ciani sitikhoza kumuona? Yesu ali m'Mwamba.
Tsiku lina pamene Yesu anadza kudzionetsanso kwa ophunzira ake, Iye anayenda nao ku Betaniya. Anawatsogolera ku phiri lochedwa Phiri la Azitona. Kumeneko analankhula ndi ophunzira ake.
Yesu anawauza, 'Muzipita kulikonse ku maiko a dziko lonse lapansi kukauza anthu za Ine. Pamene andikhulupirira muyenera kuwabatiza m'dzina la Atate ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera.'
Kenaka anawalonjeza cinthu codabwitsa kwambiri. Anati, 'Ndidzakhala pamodzi ndi inu nthawi zonse'.
Uko ku phiri Yesu sanakhale pansi ndi ophunzira ake monga ankacita. Anaima pafupi nao. Atatsiriza kulankhula anakweza manja ake kuwadalitsa.
Pa nthawi iyo pamene anali kuwadalitsa Yesu anayamba kukwera.
Ophunzira analephera kukhulupirira cimene aona. Yesu anapitiriza kukwera mpaka mtambo unabwera. Ophunzira anaona Yesu mpaka mtambo unambisa. Ndipo anadziwa kuti Iye anapita Kumwamba.
Ophunzira anatiuza nthano iyi. Anailemba m'Baibulo. Cifukwa cace tidziwa kuti Yesu ali m'Mwamba tsopano. Ndife okondwera kuti Mzimu Woyera anatsogolera Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane kuti alembe izo zonse za Yesu.
Kodi muganiza kuti ophunzira anamva cisoni pamene Yesu anacoka? Iai, sanamve cisoni. Anakondwera! Anadziwa kuti Iye ali nao nadzakhala nao nthawi zonse angakhale anapita Kumwamba.
Kodi Yesu angakhale bwanji pansi pano pamodzi ndi ife ngati ali Kumwamba? Kodi akhoza kukhala pa malo awiri pa nthawi imodzi? Inde, akhoza! Inu ndi ine sitikhoza kukhala pa malo awiri pa nthawi imodzi. Koma Iye akhoza. Akhoza kukhala Kumwamba komanso pa dziko lapansi pa nthawi imodzi.
Thupi la Yesu liri Kumwamba tsopano. Ndipo tidzamuona tikafika Kumwamba. Koma mzimu wake uli paliponse pa dziko lapansi. Sitingaone mzimu wake, koma ali pafupi ndi ife nthawi zonse. Paliponse pomwe tipita alipo. Atimva ndi kutiona. Atiyang'anira ndi kutisamalira.
Komanso, Kumwamba Yesu ayang'ana dziko lapansi nalamulira zonse zimene zicitika: zinthu zabwino komanso zoipa. Iye ali ndi dongosolo ndipo pamene Yesu atsiriza dongosolo lake anthu onse adzadziwa kuti Iye ndiye Mfumu wa zonse ndipo adzamlemekeza.

**Kukambirana**
1. Kodi tidziwa bwanji kuti Yesu anapita Kumwamba?
2. Kodi anali kucita ciani pamene anakwera Kumwamba?
3. Kodi angakhale bwanji pafupi ndi ife ngati ali Kumwamba?
4. Fotokozani citanthauzo ca 'Mfumu wa zonse'
5. Yesu aona zonse. Kodi aona ciani m'mtima wanu?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu, Tikupemphani modzicepetsa. Inu ndinu wamkulu kwambiri. Taphunzira kuti munadalitsa ophunzira anu. Mutidalitsenso kuti tizikulondolani moonadi. Mutikonzekere kuti tidzaloledwa kukhala nanu Kumwamba. Tikuyamikani kuti mumalamulira zonse. Muli ndi colinga capadera ndi zonse zimene zicitika m'umoyo wathu. Mutilimbikitse kukutumikirani. M'dzina la Yesu tikuphempani izi. Amen.

# 2. Mzimu Woyera ali ndi nchito yapadera

*Ndipo ndidzaika Mzimu wanga m'kati mwanu – Ezekieli 36.27a*

**Kuwerenga**
Macitidwe a Atumwi 2.1-8

**Malongosoledwe**
Kodi mukumbukira coonadi codabwitsa ca Mulungu comwe tinaphunzira kale kuti Iye ndiye Mulungu m'modzi komanso utatu? Baibulo litiuza za Mulungu Atate, Mulungu Mwana ndi Mulungu Mzimu Woyera.
Mulungu Atate anatilenga. Mulungu Mwana anadza kutifera. Mulungu Mzimu Woyera anadza kuti atipatse mitima yatsopano kuti tikhale ofanana ndi Mulungu.
Sitikhoza kuona Mzimu Woyera. Koma kalekale anadza pa dziko lapansi. Ico cinacitika patapita nthawi ya kukwera Kumwamba kwa Yesu.
Ophunzira ndi abwenzi a Yesu anakhala pamodzi m'nyumba m'Yerusalemu. Yesu anawauza kukhala ku Yerusalemu. 'Yembekezani mpaka Atate akutumizirani Nkhoswe', Yesu anati.
Ndiye iwo anayembekeza tsiku ndi tsiku. Sanadziwe kuti Nkhoswe ndiye yani ndipo sanadziwe njira momwe adzabwera. Anapemphera, anaimba nyimbo ndi kuyembekeza.
Ndipo pa tsiku la Sondo cha m'9 koloko anamva mau – mau akulu monga mphepo yolimba. Koma kunalibe mphepo. Iwo anayang'anirana. Ndipo anaona malilimi ang'ono monga moto. Koma ico sicinali moto. Malilime anakhala pa mitu ya ophunzira ndi abwenzi a Yesu. Ndipo mwadzidzidzi Mzimu wa Mulungu mwa iwo. Mzimu Woyera anadzaza mitima yao. Malilime ang'ono anali zizindikiro kuti Mzimu Woyera analipo.
Iwo anayamba kulemekeza Mulungu koposa. Anayamba kulankhula za Mulungu: kuti atikonda motani ndiponso kuti anatuma Mwana wake kutifera.
Anthu ena a ku Yerusalemu anamva mau monga mphepo. Anadza kuona zimene zacitika. Ndipo anamva ophunzira a Yesu polankhula za Iye.
Anthu awa anati, 'Mverani! Amuna awa ali kulankhula zilankhulo zosiyana-siyana! Alankhula zolankhulo za anthu ena onse a pa dziko lapansi. Ndipo auza onse za zodabwitsa za Mulungu!'
Anafunsana, 'Ndi ciani cimene cacitika?'
Petro anaimirira ndipo anati, 'Ndidzakuuzani cimene cacitika. Mulungu anacilonjeza kale. Mudziwa kuti Yesu anacita zodabwitsa naonetsa kuti Iye ndiye Mwana wa Mulungu. Koma Mulungu analola anthu oipa kumkhoma pa mtanda ndipo Yesu anafa. Komabe Yesu sanakhale m'manda. Akhala ndi moyo. Ndipo anapita Kumwamba. Analonjeza kutuma Mzimu Woyera. Ndipo tsono amtuma. Zimene muona ndi kumva ndizo nchito za Mzimu Woyera. Anadza kutithandiza kufalitsa uthenga wodabwitsa wa cipulumutso!'
Ico ciri nchito yapadera ya Mzimu Woyera. Apangitsa anthu kukhala ofuna kuuza za Yesu. Ndipo Mzimu Woyera apatsa anthu mitima yatsopano kuti amvetsetse ndi kukhulupirira pamene amva za njira momwe Yesu anafa kuwapulumutsa. Apangitsa anthu kukonda ndi kulemekeza Mulungu moyenera.

**Kukambirana**
1. Kodi ndi yani amene anatuma Mzimu Woyera pa dziko lapansi?
2. Fotokozani zimene zinacitika pamene Mzimu Woyera anadzaza mitima ya ophunzira.
3. Kodi nchito yapadera ya Mzimu Woyera ndi yotani?
4. Kodi munalandiranso mtima watsopano kwa Mulungu Mzimu Woyera?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu Mzimu Woyera, Lowani m'mitima yathu. Muyeretse mitima yathu ku zoipa zonse. Mutiphunzitse kuti timvetsetse uthenga wabwino wa Yesu ndiponso kuti tikhulupirira Mulungu moonadi. Tikufunikani cifukwa kopanda nchito yanu si ndife ana anu. Kopanda inu ndife otayika. Tikupemphani izi zonse m'dzina la Yesu, pakuti mwa Iye tingalandire cisomo. Amen.

## 3. Mzimu Woyera analimbikitsa ophunzira kuti ndiwo olimba mtima

*Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu – Macitidwe a Atumwi 5.29*

**Kuwerenga**
Macitidwe a Atumwi 5.25-29

**Malongosoledwe**
Kunali nthawi yakuti ophunzira a Yesu sanali olimba mtima. Ophunzira onse anathawa pamene asirikali anadza kukagwira Yesu usiku. Anamva mantha. Anaganiza kuti asirikali adzawagwiranso. Ndiye anathawa nasiya Yesu kukhala yekha ndi adani ankhanza.
Ophunzira ambiri sanalimbe mtima kulondola pamene asirikala anatenga Yesu ku phiri namkhoma pa mtanda. Angakhale anamkonda anamva mantha kotero kuti sanayende naye. Ndipo anabisala m'cipinda pamene Yesu adaikidwa m'manda. Anakhoma citseko.
Koma mukumbukira cimene cinacitika pamene Mzimu Woyera anadza kodi? Petro anaima pa maso pa anthu onse nauza iwo onse za Yesu. Anati, 'Yesuyo ndiye Mwana wa Mulungu! Muyenera kumkhulupirira kuti macimo anu akhululukidwe!' Petro sanamvebe mantha ndithu. Ndi cifukwa ciani anali wolimba mtima kotero? Mzimu Woyera wokhala m'mtima wake anampangitsa kukhala wolimba mtima.
Koma anthu amene adapacika Yesu pa mtanda sanafune Petro ndi ophunzira ena kulankhula za Yesu. Sanafune kuti iwo auza anthu kuti Yesu ndiye Mpulumutsi. Ndiye iwo anati kwa ophunzira, 'Lekani kulankhula za Yesu. Ngati musaleka tidzakuikani m'ndende!'
Petro ndi Yohane ndi ophunzira ena anati, 'Sitikhoza kuleka kulankhula za Iye. Mulungu anatiuza kuti mitundu yonse azimva za Yesu. Tiyenera kumvera Mulungu.' Ndipo anapitiriza kufalitsa.
Adani a Yesu anakalipadi. Anaika ophunzira m'ndende. Anati, 'Mawa tidzaganiza za cilango canu'.
M'mawa wansembe wamkulu anatuma asirikali ku ndende. Anati, 'Wabweretseni ku bwalo la milandu.'
Asirikali anapita mosacedwa. Anabwereranso msanga. Koma sanabweretse ophunzira. Anati kwa mkulu wansembe, 'Kulibe munthu m'ndende! Zitseko zinakhomedwa ndipo alondo analipo koma ophunzira adacokapo!'
Mkulu wansembe anadabwa. Sanadziwe zimene zidacitika.
Koma tidziwa zimene zidacitika. Usiku uyo mngelo anadza. Anatsegula citseko natulutsa ophunzira m'ndende.
Kodi ophunzira anacita ciani? Anangopitiriza kuuza anthu nthano ya Yesu. Sanamve mantha ndithu. Mzimu Woyera anawalimbikitsa.
Pambuyo pake ophunzira ena anaphedwa cifukwa anauza za Yesu. Ndipo kucokera pa nthawi iyo atumiki a Yesu ambiri anafa cifukwa ca Iye. Ndipo iwo sanamve mantha.

**Kukambirana**
1. Petro anati kuti anthu onse azikhulupirira Yesu. Kukhulupirira Yesu kutanthauza kulapa ku macimo ndi kudalira pa Yesu pa cipulumutso cake. Kodi mumakhulupirira Yesu ndi mtima wanu wonse?
2. Ndi cifukwa ciani ophunzira sanamve mantha?
3. Kodi iwo anamasulidwa bwanji m'ndende?
4. Kodi anacita ciani atamasulidwa?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu Mzimu Woyera, Mutilimbikitse kuti tizimvera Mulungu nthawi zonse, ngakhale tikomana ndi mabvuto cifukwa ca Iye. Mukhale pafupi ndi iwo onse obvutika cifukwa ca Yesu. Mutithandize kucita zabwino ndi kucita zabwino ndi kufalitsa uthenga wabwino. Tikupemphani kuti mucita tero mwa cisomo ca Yesu. Amen.

# 4. Mzimu Woyera anaunikira ophunzira

*Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa coonadi, adzatsogolera inu m'coonadi conse*
*Yohane 16.13*

**Kuwerenga**
Macitidwe a Atumwi 8.29-39

**Malongosoledwe**
Kodi mukonda kukondweretsa makolo anu? Njira yabwino yoposa yakuwakondweretsa ndiyo kukhala abwino ndi kucita zimene afuna kuti mizicita.
Mulungu ndiye Atate athu Kumwamba. Ngati timamkonda tifuna kumkondweretsa ndiponso tiyesa kucita zimene afuna kuti tizicita.
Koma tingadziwe bwanji zimene afuna kodi? Inde, tiri ndi malamulo ake; Malamulo Khumi a Mulungu. Malamulo atiuza kukonda Mulungu ndi anzathu.
Komanso kuli njira ya kudziwa zimene Mulungu afuna.
Ngati ndife Akristu oona, Mzimu Woyera akhala m'mitima yathu. Mzimu Woyera atitsogolera m'kufuna kwa Mulungu. Anatsogoleranso ophunzira a Yesu. Adzatsogolera iwo onse amene amakonda Yesu.
Filipo anali mtumiki wa mpingo. Analinso mlaliki. Analalikira za Yesu ndi njira ya cipulumutso.
Tsiku lina Mzimu Woyera anauza Filipo kupita ku njira imene inali kutali. Kumeneko Filipo anaona mwamuna woyenda pa gareta lace. Mzimu Woyera anati kwa Filipo, 'Pitani ndipo lankhulani ndi mwamunayo'.
Filipo anatamanga kwa gareta. Mwamunayo anali kuwerenga. Filipo anamva. Anamva mwamuna powerenga: 'Ngati nkhosa anatengedwa kukaphedwa… ndi monga mwana wa nkhosa…'
Mwamunayo anali kuwerenga Baibulo!
Filipo anati, 'Kodi mwamvetsa cimene muwerenga?'
Pa nthawi imeneyo mwamunayo anaona Filipo. Anati, 'Ndifunika munthu amene andithandiza. Conde, khalani pafupi nandifotokozera citanthauzo ca mau awa.'
Filipo anakondwera pothandiza mwamunayo. Anakwera gareta. Anafotokoza kuti mneneri wa kale adalemba za Yesu. Yesu anali monga nkhosa ndiponso monga mwana wa nkhosa wophedwa kukaperekedwa nsembe. Yesu anatifera.
Filipo anauza mwamunayo zonse za Yesu. Anamuuza kuti tizikhulupirira Yesu nabatizidwa.
Mwamunayo anamva mosamalira. Anaganiza kuti nthanoyo ndi yodabwitsa. Patapita nthawi anadza ku malo kumene kunali madzi. Mwamunayo anati, 'Onani, kuli madzi uko. Kodi ndingabatizidwe tsono?'
Filipo anati, 'Ngati mukhulupirira ndi mtima wanu wonse muloledwa kubatizidwa'.
Mwamunayo anati, 'Ndikhulupirira kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu.'
Iwo anatsikira gareta. Anapita m'madzi ndipo Filipo anabatiza mwamunayo.
Filipo atabatiza mwamunayo anakwatulidwa ndi Mzimu Woyera.
Kodi mwaona njira momwe Mzimu Woyera anatsogolera Filipo? Anauza Filipo malo opitako, anamuuza kulankhula ndi mwamunayo, anathandiza Filipo kufotokozera Baibulo ndipo anakwatula Filipo kukagwira nchito ku malo ena.
Mzimu Woyera ndiye Mtsogoleri wodabwitsa.

**Kukambirana**
1. Ndi cifukwa ciani Mzimu Woyera anatuma Filipo ku gareta?
2. Ndi cifukwa ciani mwamuna wokhala pa gareta anapempha Filipo thandizo?
3. Nanga inu mumacita ciani pamene simumvetsa Baibulo?
4. Kodi mwamunayo anali kuwerenga ciani?
5. Ndi cifukwa ciani ndi cofunikira kwambiri kuwerenga Baibulo?
6. Mzimu Woyera anatsogolera Filipo. Kodi akutsogoleraninso?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu Mzimu Woyera, Tikuyamikani kuti mufuna kutsogolera anthu. Mutitsogolerenso kuti tizicita zabwino pa maso pa Mulungu. Mutithandize kumvetsetsa Baibulo m'mitima yathu. M'dzina la Yesu tikuphemphani izi. Amen.

## 5. Mzimu Woyera amakulitsa Mpingo wa Mulungu

*Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu – Aroma 8.14*

**Kuwerenga**
Macitidwe a Atumwi 16.13-15

**Malongosoledwe**
Kodi mudziwa cimene cinacitika pamene Petro analankhula ndi anthu pa tsiku la kubwera kwa Mzimu Woyera? Iwo anamva bwino. Pamene Petro anati kuti Yesu wopacikidwa pa mtanda anali Mwana wa Mulungu iwo analephera kukhulupirira.
Petro anati, 'Mulungu anamuikitsa. Tinamuona atauka kwa akufa. Ndipo tsono ali Kumwamba pa dzanja lamanja la Mulungu. Yesuyo, wopacikidwa ndi inu, ndiye Kristu ndi Ambuye!'
Anthu anayamba kumva mantha. Anamva mantha poganizira kuti iwo anapacika Mwana wa Mulungu. Anati kwa Petro, 'Tidzacita ciani?'
Petro anati, 'Lapani, batizidwani ndipo macimo anu adzakhululukidwa. Kulapa kutanthauza kumva cisoni pa macimo.
Tsiku ilo kunali anthu ngati zikwi zitatu (3000) omwe anamva cisoni pa macimo ao ndipo anakhulupirira Yesu. Ndipo anabatizidwa. M'njira iyo Mpingo wa Mulungu unayamba kukula. Poyamba kunali ophunzira ocepa. Mosacedwa kunali ophunzira ambiri-mbiri. Iwo anachedwa Akristu. Ndipo izo zonse zinali nchito ya Mzimu Woyera.
Tsiku lina pamene Akristu ambiri anali kupemphera pamodzi, Mzimu Woyera analankhula m'mitima yao. Iye anati, 'Ndifuna Paulo ndi Barnaba kugwira nchito yapadera'. Paulo ndi Barnaba anali amuna Akristu abwino.
Anthu anapempheranso pofunsa Mulungu zimene Paulo ndi Barnaba ayenera kucita. Mulungu anawauza kutuma Paulo ndi Barnaba ku maiko ena kuti kumekeko aziuza anthu ena za Yesu.
Paulo ndi Barnaba anali amishioni oyamba. Anapita ku maiko ambiri. Anapita ku mizinda yambiri. Ndipo kulikonse komwe anapita Mzimu Woyera anagwira nchito m'mitima ya anthu kuti anthu ambiri anakhulupirira. Mpingo unakuladi.
Kucokera pa nthawi iyo kunali amishioni ambiri. Masiku ano kulinso anthu amene amapita ku maiko ena. Amalalikira njira ya cipulumutso. Anthu ena ayambanso kukhulupirira Yesu. Ndipo Mpingo umapitiriza kukula.
Ndi Mzimu Woyera amene amakulitsa Mpingo wa Mulungu. Athandiza anthu kufalitsa nthano ya Yesu. Ndipo Iye apatsa cikhulupiriro m'mitima ya anthu kuti iwo akhala ana a Mulungu.

**Kukambirana**
1. Kodi alaliki amacita ciani kuti Mpingo ukule?
2. Kodi nchito ya Mzimu Woyera ndi yotani?
3. Kodi tingakhale bwanji atumiki a Mulungu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu Mzimu Woyera, Ndi Inu amene apangitsa anthu kukhala ana a Mulungu. Ndi Inu yekha amene akulitsa Mpingo wa Mulungu. Tikupemphani kuti mukhale ndi iwo onse amene amafalitsa uthenga wa Yesu. Muwathandize kuti afalitse coonadi, kuti anthu ena ambiri adzalapa nakhulupirira Yesu Mpulumutsi. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu. Amen.

Mbali zina za m'buku iri zinasandulidwa kucokera ku buku ilo: Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.

- ©Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com